ATSOGOLERI OYAMBIRIRA A MPINGO

Phunziro 4 la pa July 28, 2018

Makulidwe a mpingo woyambirira anali odabwitsa. Mazana a anthu angakhale amsembe ena analowa mu mpingowu...

Komabe panauka mavuto ena pakati pa abale ndi alongo a chikhulupirirowo. Mavuto amenewa akuyenera kuonedwa komanso kukonzedwa pasanabuke kugawanika pakati pao.

Kusankha atogoleri oyenerela kunathandizira kukonza mavutowo ndi kulimbikitsa ntchito yokwaniritsa utumiki wa Mpingo.

1. Kusankha atsogoleri. Machitidwe 6:1-7.
2. Utumiki wa Stefano:
   - ⇢ Kulalikira ndi ntsutso. Machitidwe 6:8-15.
   - ⇢ Mau ndi chenjezo. Machitidwe 7:1-53.
   - ⇢ Masomphenya ndi imfa. Machitidwe. Machitidwe 7:54-8:2.
3. Utumiki wa Filipo:
   - ⇢ Samaria. Machitidwe 8:3-25.
   - ⇢ “ku malekezero ache adziko lapansi.” Machitidwe 8:26-40.

KUSANKHA ATSOGOLERI

"Ndipo mau amene anakonda unyinji wonse; ndipo anasankha Stefano, ndiye munthu wodzala ndi cikhulupiriro ndi Mzimu Woyera, ndi Filipo, ndi Prokoro, ndi Nikanora ndi Timo, ndi Parmena, ndi Nikolao, ndiye wopinduka wa ku Antiokeya" (Machitidwe 6:5)



VUTO

Mu nthawiyi ambiri mwa okhulupirira anali Ayuda, koma ena mwa iwo anali ochokera kunja kwa Yudeya. Ahelene amenewo anadandaula kuti panali kukondera mmagawidwe a thandizo la kwa a masiye awo.

YANKHO

Ophunzira analinganiza kuti asankhe atsogoleri amene ati akhale "akutumikira [*diakineō*] za pa gome" pamene ali nkudzipereka iwo okha ku "utumiki [*diakonia*] wolalikira mau." Atumiki wosankhidwawo adzitumikira ku zosowa za kuthupi ndi uzimu za ziwalo zonse za Mpingo.

ZOWAYENERETSA

Atsogoleri omwe mpingo ukuyenera kuwasankha anaayenera kukhala ndi mbiri yabwino, odzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi okhala nazo nzeru.

KULALIKIRA PAKATI PA OTSUTSA

"Ndipo Stefano, wodzala ndi cisomo ndi mphamvu, anacita zozizwa ndi zizindikilo zazikuru mwa anthu."
(Machitidwe 6:8)

Pambali powathandiza ku zosowa zao, Stefano analalikiranso kwa Ayuda omwe sanabadwire mu Yudeya.

Anakumana ndi ntsutso wolimba mu sunagoge. Posapeza chifukwa chokwanira cha kumtsutsa nacho (v. 10), iwo anadzipezera gulu la mboni zonama lomwe analilipira kuti amtsutse iye pamaso pa iwo akukhala mbwalo lalikuru loweruza milandu mu mpingo (v. 11).

Anamutsutsa iye ponena kuti anali kulalika zonyoza Mose ndi kachisi (v. 14). Ponena zotero anali kutanthauza kuti Stefano anali kunena kuti Yesu ndi Mwana wa Nkhosa amene achotsa tchimo (ndi kupangitsa anthu kusaona kufunikira kwa msembe zomwe zinali kuperekedwa mkachisi mwao).

MAU NDI CHENJEZO (I)

Machitidwe 7:1-53

"Ouma khosi ndi osadulidwa mtima ndi makutu inu, mukaniza Mzimu Woyera nthawi zonse; monga anacita makolo anu, momwemo inu." (Machitidwe 7:51)



Stefano anadzitchinjiriza yekha pamaso pa anthu onse powauza za mmene Mulungu anasamalira makolo ATHU.

Pamene bwalo lalikuru loyang'anira nkhani za kukachisi linaoneka kuti likukana uthenga wake, Stefano anasiya kulalikira.

Pamenepa anawayankhula molimbika(v. 51). Anadzichotsa iye yekha ku mbali ya atsogoleri a Ayuda pokambapo zokhudza makolo AWO. Anawauza kuti iwo anapha Mesiya monga momwe makolo awo anaphera aneneri akalero. Ndipo muchenjezo lake la Stefano munalibe kuitanira kukulapa.

Bwalo la uphungu lalikurulo linatsimikizira tsogolo la Isaraeli poukana uthenga ndi utumiki wa Stefano.

MAU NDI CHENJEZO (II)

Mau a Stefano akutsata ndondomeko ya mmene aneneri akalero anali kuitsata polankhula mau ochenjeza. Tiyeni tyerekeze chenjezo lake ndi mau a mu Mika 6.

Pangano la Mulungu ndi anthu Ake	Mika 6:1-2 Machitidwe 7:2-8	
Za mphamvu za Mulungu	Mika 6:3-5 Machitidwe 7:9-36	
Mau a mu pangano ndi kuipitsidwa kwake kwa pangano	Mika 6:6-12 Machitidwe 7:37-50	
Temberero pamene pangano liipsidwa	Mika 6:13-16 Machitidwe 7:51-53	

MASOMPHENYA NDI IMFA

Machitidwe 7:54-8:2

"Koma iye, pokhala wodzala ndi Mzimu Woyera, anapenyetsetsa Kumwamba, naona ulemerero wa Mulungu, ndi Yesu alikuimirira pa dzanja lamanja la Mulungu." (Machitidwe 7:55)

Stefano anasintha malankhulidwe ake chifukwa pamene anaona kuti munali mtsutso wankwiyo mmaganizo a ziwalo za bwalo la uphungu waukulu woyendetsa ntchito za kukachisi.

Mu nthawi yomweyo, Stefano analandira masomphenya a Yesu wokwezedwayo. Apa ndipo pamene anamvetsetsa kuti iwo omwe anali kumuweruza iye padziko lino lapansi adzaweruzidwanso tsiku lina ndi Mulungu mwini.

Anapemphera pemphero lake lotsiriza ali nkugendedwa. Pemphero la chifundo kwa iwo omwe anali kumponya miyala. Pemphero la chifundo kwa iwo omwe anali kumupha iye.

Pemphero limenero linapereka chidwi chochuluka kwa wina wochitira umboni pa imfa ya Stefano: Saulo wa ku Tariso.

SAMARIYA

"Ndipo Filipo anatsikira ku mudzi wa ku Samariya, nawalalikira iwo Kristu."
(Machitidwe 8:5)

Machitidwe 8:3-25

Atafa Stefano, Saulo anatsogolera gulu lonka lipha ndi kuzunza otsatira Yesu. AKhristu ambiri anasiya nyumba zao nathawa kuchokera ku Yerusalemu populumutsa miyoyo yao.

Filipo anatsikira ku Samariya ali nkukwaniritsa mau a ulamuliro omwe Yesu anawapereka kwa iwo (Machitidwe 1:8).

A Samaria analandira mau onse opezeka mmabukhu asanu oyambirira a mu Baibulo ndipo anali kulindira Mesiya angakhalebe chipembedzo chao chinali chosakanikirana ndi chikunja.

Koma pamene anamumva Filipo naona zozizwa zimene anazichita, ambiri analandira Yesu. Chifukwa cha ichi, Petro ndi Yohane anatumizidwa komweko kuti akaone zomwe zinali kuchitika. A Samariya ambiri analandira Mzimu Woyera chifukwa cha atumwi awiriwo, Pamenepa anakhala ziwalo za Mpingo wa ChiKhristu.

“KU MALEKEZERO ACHE A DZIKO LAPANSI”

Machitidwe 8:26-40

“Koma mngelo wa Ambuye analankhula ndi Filipo, nanena, Nyamuka, nupite mbali ya kumwela, kutsata njira yotsika kucokera ku Yerusalemu kunka ku Gaza; 'ndiyo ya cipululu.” (Machitidwe 8:26)

Filipo anaitanidwa kuchokera kuulalikira gulu lalikuru kupita kukalalikira munthu mmodzi.

Mdindo wa ku Ethiopia anafunikira kuti amve Uthenga kuti potero akaulalikire ku Africa.



Mpingo siukanasiyira kulalikira ku Yudeya ndi ku Samaria kokha. Uthenga wachipulumutso unaayenera kukafika kumalekezero adziko lapansi.

Filipo anambatiza mndindo wa ku Ethiopia natengedwa iye kupita ku Azotu. Analalikiranso mmadera onse ozungulira malo a nyanja ya mpaka ku Kaisareya. Anthu ambiri anavomereza Uthenga Wabwino napita kukaulalikira mmadera akutali.

E.G.W. (Thoughts From the Mount of Blessing, cp. 2, p. 33)

“Mu mbadwo wina uli onse wa anthu, atumiki a Mulingu anyozedwa ndikuphedwa, koma kupyolera mzisauko zao, chidziwitso cha Mulungu chakhala chikufalikira kutali. Ophunzira aliyense wa Khristu akuyenera kuimirirapo ndikutengerabe ntsogolo ntchito yomweyo ya kufalitsa uthenga, podziwa kuti adani a uthenga sangathe kulimbana ndi choonadi osakopeka nacho iwo eni choonadicho. Choonadi cha Mulungu chidzaonetsedwa kwa onse nachikhala muyezo wa chikhulupiriro angakhalebe padzakhala otsutsana nacho. Malingaliro a anthu akuyenera kuvutidwa; nkangano uli onse, za mwano ziri zonse, kuyesetsa kuli konse kowapanga anthu kusaganiza bwino za umulungu ndi njira imodzi mwa njira za Mulungu yakudzutsira maganizo a anthu ku turo tawo kuti akalalikire za choonadi cha Mulungu.”